

JOYCE
MEYER

TINGAPULUMUTSIDWE BWANJI
KU CHISOKONEZO

Chifukwa,
Mulungu,
Chifukwa?

Unless otherwise indicated, all Scripture quotations are taken from
THE AMPLIFIED BIBLE: Old Testament.

Copyright © 1962, 1964 by Zondervan Publishing House
(used by permission); THE KING JAMES VERSION; and from

THE AMPLIFIED NEW TESTAMENT

Copyright © 1958 by the Lockman Foundation
(used by permission).

Copyright © 2014 by Joyce Meyer Ministries – South Africa

All rights reserved. No part of this publication may be
reproduced, distributed, or transmitted in any form or by any means,
or stored in a database or retrieval system, without the prior written
permission of Joyce Meyer Ministries – South Africa.

Joyce Meyer Ministries – South Africa
PO Box 5, Cape Town, 8000

Phone: +27 (0) 21 701 1056
Website: www.joycemeyer.org

Go to tv.joycemeyer.org to watch Joyce's messages in a
variety of languages

Why God Why? - Chewa

Not For Resale

ZA MKATIMU



<i>Liwu Loyamba</i>	4
1. Chimapangitsa Chisokonezo Ndi Chiyani?	5
2. Kumasulidwa Ku Malingaliro	8
3. Makhalidwe A Chikhulupiliro	10
4. Chisomo Chimabwela Tsiku Limodzi Pa Nthawi	12
5. Kukanakhala Ngati	15
6. Nanga Ngati?	17
7. Musatsogozedwe Ndi Malingaliro Anu	20
8. Malingaliro Amabweletsa Chinyengo	24
9. Chisokonezo Chimaba Chimwemwe Chanu	28
Pemphero la Chipulumutso	30
Za Olemba Bukhuli	31

LIWU LOYAMBA



Yohane 10:10 (AMP) ikuti sikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga, koma Yesu adza kuti mukhale ndi moyo ndi kukhala nao wochuluka.

Mdielekezi akufuna abe chimwemwe chako kenoka akuletse kuti usasangalale ndi moyo wako. Koma ndi pemphero langu kuti bukhuli likuthandize kuphunzira “kumusiya Mulungu akhale Mulungu” pamoyo wako, kuti usangalale ndi mtendere wochuluka ndi chimwemwe kuti Yesu anakufera kuti ukhale nacho.

1



CHIMAPANGITSA CHISOKONEZO NDI CHIYANI?

Kodi, mwasokonezeka? Kapena pali china chake chachitika moyo wako, moti siukutha kumvetsetsa? Mwina ndi kale lako, ndiwe sukutha kumvetsa chifukwa chani moyo wako unalili bwanji. Kapena umanena, “Chifukwa chani ine Ambuye? Chifukwa chani zinthu sizimachitika chonchi kapena chonchi? Ndi chifukwa chani zinthu zasintha motele? Sindikumvetsa!”

Ndinayamba kuzindikila anthu ambiri amabvutika kwambiri ndi chisokonezo. Ndinadziwitsidwa kale ndi kudziwa m'mene anthu amakhuzidwila ndi chisokonezo, ndinayamba kuganizira kuti m'chifukwa chani anthu amasokonezedwa, ndipo anapange bwanji kuti aziteteze.

Usiku umodzi ndinali ndi msonkhano ku Kansas City, koma anthu okwana mazana atatu anabwera. Ndinamva kuti ndinfunse kuti ndi anthu angathi mwa iwo amene anasokonezedwapo ndi nkhani dzina pa moyo wao. Modabwitsa, ndinaona anthu awiri okha amene sanayimike manja awo, modzi mwa iwo ndi amuna wanga.

Ngati ndinaona bwino, dzikuthantauza kuti anthu 298 mwa anthu 300 anali wosokonezeka. Ndiye ngati 99.3%. M'mene ndinayamba kuonana ndi magulu wosiyana siyana ndinapeza kuti ili ndi bvuto kwina kuli konse.

Pamene nditadziwa izi ndinayamba kumfunsa Mulungu kuti andionetse chimene chimapangitsa chisokonezo. Anati, “*Auze asiye kuyetsa kuzipezela yankho ndipo sazachalanso wosokonezeka.*” Tsopano ndikuzindikila ndi chifukwa chake sindimabvutika ndi chisokonezanso. Ndili ndi zinthu zambiri m’moyo wanga zimene sindimadzimvetsetsa koma pali kusiyantiso kwa kukulu masiku ano. *Mulungu anandimasula kumbali yazipezeza yankho ndekha, komanso ku maganizo* (“maganizo” amene 2 Akolinto 10:5 ifotokozerana), choncho sindizayesa kuzipezera mayankho m’moyo wanga pa zinthu zimene sindimazimvetsetsa.

Zikumveka ngati ndi zopweka, sichoncho? Koma pali kumasulidwa kweni kweni kuchokela ku mtsautso wa chisokonezo pakukana mayeselelo azipezela mayankho (chifukwa). Ngati mungasiye kulingalila ndizomveka, chifukwa zonzezi zimachokela mu m’malo otchedwa “malingaliro” olo “maganizo.”

M’maganizo ndi malo akhondo kumene timamenyana ndi mdielekezi. Tikhonza kupambana kapena kulephela. “*Mulungu simwini wa chisokonezo*” (1 Akorinto 14:33) – ndi mdielekezi amene amatipatsa maganizo amene sali olingana ndi Mau a Mulungu. 2 Akolinto 10:4, 5 (Amp) ituza kuti ndi chinthu chimodzi chimene tikuyenera kulimbana nacho kuti tikapambane ndi maganizo. Ndimeyi imati:

“Pakuti zida za nkondo yathu siziri za thupi [za nyama ndi magari]. Koma za mphamvu mwa Mugulung za kupasula malinga, ndi kugwetsa pokana chidzwitso cha Mulungu, ndi kugonjetsa ganizo lonse ku kumvera kwa Khristu (Mesiya, Wodzodzekwayo).”
2 Akorinto 10:4, 5.

Ngati Mau atiuza ife kuti tisayese kuzipezela mayankho patokha, tiyenela kumvera. Pamene maganizo abwela, tipeleke malingaliro athu amvere Yesu. Mau akunena tili mu nkondo yomenyana ndi maganizo. Mdielekezi akulimbana ndi malingaliro athu.

Molingana ndi malemba tikulimbana ndi machenjelelo ake ndi *malingaliro*. Munganizilapo za zinthu zomwe zili zonama kapena kuona zinthu za m’malingaliro zomwe zili zosayenela? Machenjelelo ndi maganizo za

kuzipezela mayankho patokha, ndi malingaliro ndi maganizo amene afuna funa kuyankha mafunso amene Mulungu yekha akhonza kuyankha.

Pomariza, tikhonza kunena kuti kusokonezeka kumabwera ndi kuyesa kuzipezela mayankho patokha kwa chintu chimene Mulungu yekha akhonza kuyankha. Pali zifukwa zina zimadziwika kwa iye yekha koma satiudza.

2



KUMASULIDWA KU MALINGALIRO

Choyamba mukhoza kuona kuti ndi maganizo anji amene ndinali nawo musanakhutile kweni kweni za kuwomboledwa m'malingaliro. Kale m'moyo wanga ndinayesa kusadali munthu ndi kukhala ndi kuzisamalila ndekha chinali chinthu chofunikila kwambiri pa ine. Ndinaganiza kuti laling'ono thandizo limene ndipeze likhala bola chifukwa sindikhala ndi ngongole ndi munthu. Ndinali otopa ndi m'mene zimandpweteka, ndipo ndinaganiza kuti kodi mchtidwe otolowu ungandithchinjilize m'kupwetekedwa kwanga.

Ndinali ndi wolakwa koma zinanditengola nthawi kuti ndidziwe ndi kubvomeleza izi. Poti zinatenga nthawi yayitali. Zinanditengelansa zaka zambiri kudandaula, kulingalira, kuganizira, kutsinkhatsinkha, kufunafuna, kukhumudwa, kuzunguzika ndi zina zotele. Pamene ukuzidalira kwambiri wekha mpobvuta kumukhulupilira Mulungu kapena wina wake.

Mulungu akufuna tumudalile Iye osati kusamudalila Iye, pofuna kuzidalila tokha. Paene tikumudalila Mulungu kwambiri, ndipamene timayamba kuzindikila zinthu mwa Iye, zimene sungazimvetsetse. Ndikuziwa kuti akudziwa ndipo pamene nthawi yoyikikayo azazibvumbulutsira kwa inu.

Musasokonekele ndi malingaliro akale, sityenela kumaganiza za mbuyo malingalila ndi chikhulupiliro. Ngati china chako chachitika m'moyo

wako kwa iwe kapena mzako zoti sukuzimvetsetsa. Konse kuti zathka bwanji? Kapena ndi chifukwa chani. Choyambilira chikhale pemphero. Mfunsemi Mzimu Woyera akupatse kumvetsetsa, kukuphunzitsa, kukuwonetsa kuwala ndi kubweletsa bvumbulutso kenako kudikila pakana atakwanilitsa. Ndikudziwa kuti nthawi ya Mulungu yoyikikayo azabweletsa kumvetsetsa.¹

Pamene mfunso labwela mu mtima mwako, umasinkhasinkha pang'ono koma mu nyengo yomweyo umayamba kumva kusokonezeka. Chofunika mthokoze Mulungu chifukwa ali ndi yankho, muwuzeni kuti ndinu wokutila kudziwa kuti ukumudalira Iye kuti akuwonetsa m'nthawi yake ya bwino.

Sungamasulidwe m'malingaliro ndi chisokonezo pokha pokha utachila ndila. Machitidwe amene ndakhala ndikuwakamba, ndi *makhaliidwe a chikhulupiliro*.

1 Joyce analemba bhuku limene lifotokozerana nthawi ya Mulungu, lichechwa “Liti, Mulungu, Liti?”

3



MAKHALIDWE A CHIKHULUPILIRO

Tingafotokoze kuti chikhulupiliro ndi chiphunzitso chimene timalandila kuchokela kwa Mulungu. Pa Aefeso 2:8, 9 tikuona kuti mwa chisomo *kudzera m'chikhulupiliro* tinapulumsidwa. Ahebri 11:1 (AMP) ikuti, "Chikhulupiliro cha zinthu zasayembekezeka, kukhala ndi chitsimikizo cha zinthu zomwe sitinazione." Tingalongosole za chikhulupiliro mu njira zambiri, koma ndi makhulupilira pali njira yophweka yo yang'ana za chikhulupiliro, pena kuziona ngati zikupanga zinthu m'chikhulupiliro kapena ayi, nkunena kuti "chikhulupiliro chili ndi makhalidwe."

Makhalidwe a chikhulupiliro chimabweletsa ife ku mpumulo. Ahebri 4:3 ikuti kwa ife amene takhulupilira tilowa mpumuluwo (kumbukilani chikhulupiliro ndi njira ya mpumulo) adapumulanso mwina wake Mulungu ku ntchito zake. (Ndime ya 10). Malingaliro ndi ukapolo ndipo umakutengela ku chisokonezo osati mpumulo.

Makhalidwe a chikhulupiliro ndi kutaya nkhawa zanga zonse pa iye pakuti iye asamala (1 Petro 5:7) *ikuti sindifuna kudziwa kapena kubvetsetsa m'mene zinthu zikuyendela, chifukwa ndi makhutitsidwa kudziwa amene akudziwa zinthuzo*. Khalani ndi nthawi yanu yofuna kumudziwa iye koposa kufuna kudziwa zimene akulingalira.

Makhalidwe a chikhulupiliro ndi kosadandaula kapena kukhala ndi mantha, osadela nkhawa za mawa, chifukwa chikhupiliro chimazindikilitsa kumene tiyenera kupita ngakhale zinthu zosadziwika za mawa. Kumbukilani kuti

ndi amene analipo, alipo, ndipo azdakhhalapo. Analipo madziko a dzika lapansi asanakhazikitsidwe. Ndi mwini chilengedwe. Anakudziwani inu musanabadwe. Anakulengani iye ndi manja ake m'mimba ya mai anu. Osati anangokhala pa chiyambi, koma iyeyo ndiye chiyambi, woyamba, Alefa.

Ndiyenso mathelo? Kodi amayamba zinthu kenako nkuzisiya? Ayi! Amamaliza zimene waziyamba (Aheb. 12:2; Afil. 1:6). Adzakalapo pakana pamathelo. Ndiye mathelo. Wotsiliza, ndi Omega. Ndimakonda kuyankhula motelo “Sindiye Alefa ndi Omega, chiyambi ndi chitsilizo chokha, komanso ali pakati.”

Kungolingalira kuti Yesu wachedwa pang'ono ndili ndi tsiku lamawa lotsala, chimodzi modzi inunso ndili wa chimwemwe ndi kukhala wotonthozedwa ndi kudziwa. Taona ndakulemba iwe pa zikhato za manja anga. (Yes. 49:16).

Makhalidwe a chikhulupiliro amakhala tsiku limodzi panthawi.

4



CHISOMO CHIMABWELA TSIKU LIMODZI PA NTHAWI

“Malingaliro” amatha kutibweletsa mbuyo kapena kuyesa kutikankhila ku tsogolo. Kumbukilani Baibulo limati “chikhulupiliro ndi *tsopano*” (Aheb. 11:1). Mukamayesa kukhala ndi makhalidwe a mbuyo, moyo udzakhala wobvuta. Sanazitchule yekha kuti ”wopambana amene ndi za khale.” Mukamayesa kukhala ndi makhalidwe a tsogolo, moyo udzakhala wobvuta. Sanazitchule yekha kuti “wopambana amene ndizakhala.” Koma ukhakala tsiku limodzi pa ka nthawi, tsiku limene ulili ndi tsopano, moyo ukhala wophweka. Anati “ndine” Ekso. 3:14. Chikhulupiliro ndi *tsopano*.

Anawauza ophunzira ake m’mafundo “chifukwa chani mukuopa? Limbani mtima, NDINE!” (Mat. 14:27). Mukumvetsetse? Yesu ananena ndili pano ndi inu tsopano, pamene “ndili” zonse zimakhala bwino. Khalani mu za lero! Kudandaula za dzulo kapena mawa kumaba tsiku lako. Tapatsidwa chisomo tsiku la lero. Chisomo cha mawa sichingabwele pokha pokha titafika mawalo. Komanso chisomo cha dzulo chagwilitsa kale ntchito. Chisomo ndi chothekela kukondeledwa ndi mphamvu za Mzimu Woyera umatithandiza kukwanilitsa zonse zofunika kuchita. Koma sitingapeze chisomo nthawi yake isanakwane kuti tisungiletu ayi!

Kumbukilani ana Aisrayeli m’chipululu Mulungu modabwitsa anawadyetsa tsiku lili lonse pogwetsa chakudya kuchokela kumwamba.

Amatchula kuti “mana.” Ngati ifenso, iwowa amayesesa akhale nacho chokwanira lero pakana mawa. Amafuna akhale nacho chakudya chokwanira mawa kupangira kuti mwina Mulungu angaiwale kutsitsanso madalitso wa zakudya koma Mulungu anawachenjeza kuti asatole moposa muyezo wa ali yense patsikulo, kupatula la sabata. Koma amati akatola muposela muyezo, zimaonongeka.

Tikakhala chete ndi kuganiza pang’ono, ndi chitsanzo cha mphamvu choti tikhonza kuchiyika a miyoyo yathu lero. Pamene tikulingalira, kudandaula zili ngati kuyesa kusunga mana wa mawa? Atate wanu wa kumwamba akufuna mukhulupilira pa za mawa. Miyambo 3:5 (AMP) ikunena za kumukhulupilira Yehova, ndi mtima wako wonse osadalira pa luntha lako.

Ndinawelenga pena pake ndondomeko zingapo. Azibabmo awiri anali mu ndende chifukwa choyikila umboni wa Yesu Khristu. Amayenera awotchedwe m’mamawa wake. M’modzi mwa iwo anali wamkulu wopatulika amene amamudziwa Mulungu ndi njira zake. Winayo anali mnyamata amene amakonda Mulungu kwambiri koma samadziwa zambiri za njira za Mulungu.

Mnyamata amayatsa matchesi ndi kuyatsa kandulo, kutayamba mdima m’mene anayatsa mdima unachulukila ndipo anaziotcha chala; nayamba kukhumudwa ndi kukuwa mwa mantha ndi kunena, “Ngati kuziwotcha chala kukupweteka chonchi sindingathe kudikila kuti ndiwotchedwe patsikulo.” Wamkulu wopatulikayo anamulimbikitsa ndi mau awa, “Mnyamata, Mulungu sanakuuze kuti uziwotche chala choncho ndiye kuti sunalandile chisomo. Akufuna uzipelke nsembe ku moyo. Ndipo uzakhala wotsimikizidwa kuti pamene m’mawa ukadza. Chisomo chizakhalapo kuchita chimene ukuyenela kuchita.”

Mwaona wankuluyi anadziwa zambiri ku dzaka zimene anayenda ndi Ambuye, kuti pamene walephela, mawa likafika chisomo chimakhalaponso. Choncho anonthozedwa tsopano. Chifukwa anali ndi chikhulupiliro cha tsopano, kuti mawa nkothekela kuti chisomo chizakhalaponso.

Mukuona chitsanzo ichi cha chikhulupiliro chatimasula ife mu “malingaliro.” Chikhulupiliro sichifunika kuganiza za mtsogolo.

Chikhulupiliro chimapulula chifukwa chimadziwa kuti Mulungu abweletsa mana a mawa. Ndikulimbikitsani kuti musaononge nthawi yanu lero kufuna kulingalira zimene zinachitika kale kapena zimene zinzachitika mtsogolo.

Monga m'mene ndinwelenga, dzulo lili ngati cheke chopanda ntchito, mawa ndi tsiku lolonjezedwa ndipo lero ndi tsiku lolandila. *Ligwelitseni bwino ntchito!*

5



KUKANAKHALA NGATI

Mtumwi Paulo amaphunzitsa ku aphilipi kuti tikuyenela kusiya zimene zili zambuyo ndi kuyang’ana patsogolo (Afil. 3:13). Kodi, tingakamile bwanji zinthu zambuyo ngati si malingaliro athu? Tikhonza kusiya kukhala ndi maganizo ambuyo.

Kenaka mphamvu zimenezo kugwiritsila ntchito lero kodi mu makhalabe mu zolakwika za mbuyo nthawi zonse? Kapena umaganiza “Chifukwa chani ndinanena kuti? Kukanakhala sindinananene kapena kuchita.” Kapena, “Ndikana kuchita ici kapena icho.” Samalani ndi mau oti *“ndikana.”*

Mwina mumaganiza kuchita zinthu koma sizikuyenda m’mene zimayenera kukhalira. Kapena mumaganiza “Chifukwa chani zinthu zikuyenda chonchi? Chifukwa, Mulungu, chifukwa? Sindikuzimvetsetsa. Ndiyenera kuziona bwino! Sindingakhale osazindikila! Oo, koma ndasokonekela!”

Kodi, maganizo anu ndi otero? Ndikhonza kukhalabe ophinjika? Mukungozidzunza nokha! Ndakhala dzaka zambiri ndichita izi koma sizimagwila ntchito! Panali zinthu zambiri mbuyomu zomwe ndimachita, koma mpaka pano sindimazimvetsabe. Koma ndikuthokoza Mulungu kuti anandiwuza kuti ndikuyenera kusiya kuyang’ana mbuyo ndi kuyang’ana mtsoغو. Pano ndimasangalala ndili ndi mtendere woposa.

Mau akunena ku Yesaya 26:3 kuti “Inu muzasunga mtima wokha zikika mu mtendere weni weni chifukwa ukukhulupililani inu.” Sananene kuti amene malingaliro ake ali otanganidwa ndi kulingalira kuyesa kuwelengela zinthu zonse azasungidwa mu mtendere weni weni ayi.

Pali zinthu zowoneka, zosakhala bwino zomwe zimachitika mbuyomu. Ndi m’mene zimakhililanso ndi inu; zinthu zambiri zimachitika kwa inu zimene sizinali zoyenera. Zimene zimabweletsa mabvuto, mabala ndi kupwetekedwa. Zimene zimatenga zaka kuti zichoke.

Ndinakhala zaka ndi chisoni, kuwawidwa ndi kuyesa kuganiza mchifukwa chiyani anthu sanandithandize. Chifukwa cha chiyani Mulungu sanandithandize? Chifukwa cha chiyani kunalibe munthu amene anandithandiza?

Ndinazindikila kuti ndikuzipanga ndekha kukhala wokhumudwa, ndimawononga tsiku langa kuyesa kumvetsetsa za dzulo. Tsiku lina Mulungu anandinong’oneza, “Joyce, ukhoza kukhala wa chisoni kapena wamphamvu. Ndi chiyani ukufuna?”

Nthawi zina mukhoza kukhala mu chigonjetso cha dzulo. Ukhonza kukhala ndi kuganiza chimene unachita kuti upambane, kuti uzachitenso. Ndinazolowela *kusewela* ndi malingaliro, mu chigonjetso cha mbuyo. Ingakhale zimenezo zikhoza kukuletsani kupita chisogolo. Zakale ndi zakale; zilibe ntchito kuti kalero linali ndi chigonjetso kapena ayi, ndi zakale basi, zinapita. Khalani mu *zalero!*

Palibe cholakwika kulingalira zakale, koma ndikolakwika *kukhala* mu chigonjetso cha kalecho. Patatha chosangalatsa m’moyo wako, usiyeni zipite pamene mukudikilira zinthu zina, zimene Mulungu alinazo pa iwo. Afilipi 3:13 (AMP) ikuti, “Poiwaladi zam’mbuyo ndi kutambalitsira za mtsogolo.”

Ndifuna kubwelezanso kwa inu kukhala osamala ndi mau oti “*ndikana.*” Ngati choyipa chachitikia, timapezeka tikuganiza kuti *ndikanachichitanso* kawiri. *Iwalani za mbuyo!* Musaganizelenso. Pangani chisankho lero kupita mtsogolo.

6



NANGA NGATI?

Chida china champhamvu (Baibulo pa Aefeso 6:16 ndi ”mbivi yoyaka”) imene Satana amaiponya kwa inu mu mantha imabweletsa maganizo a, *nanga ngati?*

Nanga ngati ndalama sizibwela lero? *Nanga ngati* ndingapwetekedwe? *Nanga ngati* nditadwala kwambili? *Nanga ngati* ntchito itatha? *Nanga ngati* nditakhala ndekha moyo wanga wonse? Kapena bwanji izi, *nanga ngati* sukumvetsela kwa Mulungu? *Nanga ngati* ndingalakwitse? *Nanga ngati* mungalephele? *Nanga ngati* anthu atakusekani? *Nanga ngati* utakanidwa? Ndi zina mukuzindikila maganizo amenewa?

Nanga ngati ndi njira yinanso yoyesa kuwelengera zinthu pa *kulingalira* mau oti. *Nanga ngati* akabwela nthawi zambiri amatibweletsela chithunzithunzi chokayikila. *Nanga ngati* amatitengela ife mtsogolo ndi kutipangitsa ife kuopa zinthu zimene sizinachitike koma pokha pokha titadzichita mu mantha zokhonza kuchitika.

Nanga ngati akubweletsa chisokonezo monga *ndikanakhala ngati*. Zonsezi ndi njira imodzi yolingalila kuti sitikuyenela kupeza zofuna zathu. Sitikuyenela kupeza zofuna zathu. Zonsezi zinaonjezedwa mu 2 Akorinto 10 muli dongosolo la malingaliro, maganizo kuyelekeza. Zonsezi zikuyenela kusiyidwa.

Dikilani ndikupatsani chitsanzo za zimene ndikutanthauza. Tsiku lina

utumiki wathu unafunika kuti timange malo ophemphelamo. Moti tinayenela kuleka kaye makumanidwe athu apa sabata. Momwe tinakumanila kupitilila zaka zisanu zapitazo inagwa mu zaka ziwiri. Ndipo malo ogulitsila dzinthu anayenera kukhala m'malo mwake. Tinafunana malo amene pangakhale nyumba. Malo ogwirilamo ntchito, makumanidwe anthu apa sabata ndi malo ena okelelamo ana. Utumiki wa ana ndi malo ena akulu ndi zina. Komanso tinafunana kukhala ndi pokhala magalimoto okwana 300.

Ndiyeno wina akhonza kuganiza kodi sizingakhale zobvuta kupeza, komabe sizinali zopweka m'mene mukuganizila ayi. Tinakhala tikuyang'ana kwa zaka ziwiri. Tinatopa ingakhale panali ma mwayi wosiyana siyana amene tinawadziwa. Zinaoneka ngati tafika pamathelo.

Satana anaponya mibvi yake ngati iyi, “kodi, nanga ngati zaka ziwiri zitadusa asapezabe malo?” Kapena mibvi wina unabwela utatenga nkhani: “Kukanakhala ndinatenga ichi ni ichi m'mene zinthu zimapezeka zotchipa sindikanakhala mu nyengo imeneyi. Nanga ngati utamusowa Mulungu? Ndikanakhala ndikudziwa mitundu ya zinthu, ndikanadziwa chimene tikuyenera kuchita. Nanga nditagula dzinthuzi koma osapeza chiloledzo chomwe tikufuna? Nanga mutapeleka ndalama zambiri kenako ndikupeza china cha bwino chotsika mtengo?”

Pafupi pafupi ndimathokoza Mulungu kuti ndinamasulidwa ku ukapolo wa malingaliro isanafike khani ya kufuna nyumba. Ikanakhala nyengo imeneyi inachitika zaka zapang'ono zathazi. Ndinakakhala m'moyo wobvutika, wosokonezeka ndi wa m'mantha pa kuyesa kuwelengela zinthu zonse.

Ndikhulupilira tsopano kuti Mulungu akhazikitsa mayendedwe a munthu (Masal. 37:23). Tikupemphela ndi kukhulupilira Mulungu, ndipo tikufuna chifunilo chake. Choncho atitsogolera ku malo oyenelera ndi mu nyengo yake. Mulungu safulumila komanso sachedwa, pali njira zambiri zomwe tayesesa mbuyomu zimene sizinayende. Zinalibe ntchito kutitayesesa bwanji. Choncho, mu nthawi yake Mulungu wokwanilitsa ndi malo a bwino okhalapo. Ndipo apitiliza kukwanilitsa chili chonse.

Pano ndikutha kuwona ndi kusiyanita zinthu ndi kuona ndi chifukwa chani sizimayenda bwino. Koma panthawiyi sikuonetsa ngati ndimayesa ndi mphamvu kupeza malo palibe chimayenda. Palibe chimayenda pamene tili kutali ndi nyengo ya Mulungu, kuyesa *kupanga* zinthu kuti zichitike.

Mulungu amadziwa chimene akuchita. Ali kutitetedzabe ndikhonza kumadikila ndi kudziwa kuti ingakhale ndisakuziwa chimene ndikuyenela kuchita, ndikumudziwa amene amadziwa zonse.

Sindikudziwa za inu? Mukumudziwa Yesu? Ndiye kuti mukumudziwa odziwa zonse. Wamphamvu zonse. Opezeka pali ponse.

Pumulani! *Nanga ngati* mukhonza kulingalira lingalira, komaliza ndi kuganiza kuti ndawelengela zonse kenako. Mulungu kukudabwitsa ndi kuzichita mu njira yake yake? Ndikudziwa kuti nthawi yonse ija ikanakhala yopanda ntchito. Simunatayepo nthawi yanu kulingalira ndi kusokonezeka?

Ayi ndi maganizo abwino: *Nanga ngati* osangopumula ndi kumusiya Mulungu akhale Mulungu?

7



MUSATSOGOZEDWE NDI MALINGALIRO ANU

Ndimapemphela chidziwitso kuti chigwile ntchito mu moyo wanga koma mu muyeso waukulu. Kungoti ndakhala ndikumphempelela kwa nthawi yaitali pamene Mzimu Woyera unandilankhula. “Sungakhale ndi chidziwitso Joyce, pokha poka usiye kulingalila.”

Akorinto woyamba 2:14-16 imatiuza mwachindunji kuti munthu achibadidwe cha umunthu salandila za Mzimu wa Mulungu. Ambuye wagwilitsa ntchito ndimiya kuti mau amveke bwino. Ngati mzimu wanga wabweletsa chidziwitso ndiye mutu wanga ukulingalira kuona kuti ndi zoon kapena ayi. Sindingapite patsogolo. Chifukwa chani? Chifukwa cha dzimene 1 Akolinto 2:14 ikunena: Munthu wachibadwidwe cha umunthu sangamvetsetse zinthu za uzimu chifukwa mzimu wako umadziwa zinthu zimene malingaliro ako sakudziwa.

Ngati uli wobadwanso mwatsopano mwana wa Mulungu, pamenepo Mzimu Woyera umalowa mu uzimu wako waumunthu. Ndikhulupilira Mzimu Woyera ndipo amatiuza zinthu zomwe nthawi zambiri sitimafuna kuzichita chifukwa timagwiritsa ntchito umunthu.

Ndikupatseni chitsanzo. Tsiku lina m’ mawa ndikukonzeka kupita ulendo wokakumana, kumene timakumana sabata lili lonse ku “Umoyo mu Mau (Life in the Word)” ndinayamba kuganiza za mzimayi wina amene

amatsogolela utumiki wotheandiza ndi m'mene analili wokhulupilika. Chikhumbobhumbo chinadzuka m'moyo wanga kuti ndimuchitile china chake kumudalitsa njira yina yake.

Ndinanena, “Ambuye, ndingachite chiyani kwa Ruth Ann?” Ndinamva mphamvu mkati mwanga olo mukhoma kunena ndinaziwa kuti ndimafuna kumpatsa diresi yanga yofiira imene ndinayisunga. Diresiyi ndinayigula miyezi itatu yapitayo. Ngakhale ndimaganiza zoivala koma ndinalibe chikhumbobhumbo choivala. Inangokhalabe mpepala m'mene inalili kuchokela ku sitolo. Ruth Ann anali wang'ono wanenepako kuposa ineyo, koma chotsangalatsa inamukwana, ndinagula diresiyi yaikulu kuposa imene ndimabvala chifukwa kunalibe mulingo wanga. Ndi m'mene mapangidwe ake a diresi analili ndikukhulupilira kuti palibe amayiwana kuti ndiyayikulu.

Pamene chilakolako chinakula pa moyo wanga kuti ndipeleke diresiyi malingaliro anga anati koma “Ambuye diresi ija ndi yatsopano.” Mudziwe kuti ngati malingaliro anga aumunthu akukangana ndi mzimu wanga. Mkanganowu okhonza kukhala wobvuta kwambiri. Kenako ndinati “Zoonu ukundiuzwa kuti ndisapereke diresi yatsopanoyi.” Choncho ndinakaganiza za makhalidwe a Mulungu, machitidwe ake ndi kupambana kwake, ndinakadziwa kuti Mulungu akundiuzwa kuti ndipeleke diresi yatsopano osati ya kale.

Mfumu Davide inati pa 2 Samueli 24:24 ikunena za kumanga kachisi, “Pakuti sindizapeleka kwa Yehova Mulungu wanga nsembe zopsereza zopanda mtengo wake.” Mukuona thupi lathu silimasamala kukhala pamodzi ndi zinthu “zopanda ntchito” kwa ife. Mwa choncho nkhani ya diresi yofiira ndi nkhani yosiyanyanako. Kutu ndizisiye izi ndinayenela kupeleka nsembe.

Mtsutsano womalizawu unali wosekesa ndinati “Ambuye, ndinagula ndolo zokongola zofiira ndi za siliva kuti ndidzibvala pamodzi ndi diresiyi.” Ndinayankhula izi mwa manyazi, ndimaganiza kuti Ambuye andimvela chisoni koma yankho lake linali kungokhala chete pa mtsutsano umene ndinali nawo. Poyikila ndimanga zokhuza ndolo, anandidziwitsa kuti ndikana thanso kupelekanso ndolozo ngati unali ndi bvuto pozisunga

popanda diresi.

Mulungu samalimbana nafe. Amatiuza mwa *chifuniro chake poikiza mu uzimu wathu mau achetechete, nthawi zina mau omveka koma nthawi zambiri kuzela m'malemba mu mau ake amene amatilankhula ife*. Kumbukilani, Mulungu sadzakutsogolelani kuti muchite chinthu chomwe sicholinga chake, chimene chili mau ake. Komanso samalani ndikutsogozedwa ndi zomwe mwamva. Pali mau ochuluka. Muonetsetse kuti mzimu wanu ukukuyikilani umboni za Mzimu Woyera.

Mzimu wanga unaikila umboni za Ruth Ann kuti atenge diresi, koma thupi langa silimafuna. Ndiye ndinapeleka ngakhale zinali zosamvetsetseka koma ndi chifukwa cha Mulungu. Komano Mulungu sanalimbane nane. Wayankhula zimene amafuna kuyankhula. Ngati mukukumbukila m'mene zinayendela poyamba ndimaganiza za Ruth Ann kuti anali mdalitso. Ndiye ndinamfunsa Mulungu ndingachite chani pa iye. Anandiuzwa, koma mutu wanga (*malingaliro* anga) samalola ingakhale mzimu wanga umadziwa kuti ndi chabwino ndiye zinali kwa ine *kusankha*.

Ndiye ndinataya malingaliro anga. Ichi ndi chisankho chabwino kuti tichite chimene Mulungu akutiuzwa pokana kusamvela. Choncho chidedo ndi kusamvela. Malingaliro abwino sikumvela, koma mchitidwe wotengedwa kuchokela m'mau a Mulungu ndiye kumvela.

Masabata angapo apitawo, ndinayiwala za nkhani yonse. Koma Mulungu sanayiwale. Ndimamupemphela Ruth Ann, ndiye anakhala ndikuyankhula zomwezo kwa iye nthawi zambiri, “Ambuye, ndingamudalitse bwanji Ruth Ann?” Aka kanali kenanso. Diresi yofiira yomweyija inabwelanso mkati mwanga. Komaliza ndinazindikila kuti sindimabvela Mulungu ndinapeleka diresiyo.

Kuti ndichifukwa chake imangokhala pachingwe kwa miyezi itatu ine osayitengapo olo kuyichotsa mpepala yake. Mulungu anali atadziwa zonsezi kale. Tikhonza kuzichita pa kumvela zolakwika zonsezi zikuchita chifukwa cha umunthu posamvetsetsa za umunthu wa uzimu umene 1 Akolinto 2 unanena.

“Chifukwa, Mulungu, Chifukwa?” Umunthu umanena “Chifukwa chani mukufuna ine ndipeleke nsembe? Chifukwa chani sizopweka? Chifukwa chani zili zobvuta chonchi?” Aroma 8:6 (AMP) ikuti maganizo a thupi ndi opanda phindu ndi maganizo opanda Mzimu Woyera. Imationetsela kuti ndi mtundu wa makhaliidwe awa umaba mtendere wathu.

Mwina mwayiwala cholinga cha bukhuli, ndikukumbutseni poyesela kukhazikitsa kuganiza kwakuti “Chifukwa, Mulungu, Chifukwa?” ndi chinthu chimodzi chimene chimabweletsa chisokonezo, kuba mtendere, mathelo ake kulanda chimwemwe chatu.

Mukufuna kukhala wosangalala? “Malingaliro akuyenera kuchoka!”

8



MALINGALIRO AMABWELETSA CHINYENGO

Chinthu chimodzi chofunikila kuti tisanyengedwe masiku ano ndi pakuyenda ndi mzimu – kutosogozedwa ndi mzimu, osati mu thupi. Mdyelekezi akuyang’ana Akhristu amene akutsogoleledwa ndi malingaliro awo m’machitidwe awo ndi chifuniro chawo koposa mau ndi Mzimu Woyera. Sitingapangeko kanthu chifukwa timamva choncho kapena osamva choncho. Tikuyenela chifukwa cha ufumu ndi chitetezo cha ife tokha tipange chinthu chimene Mzimu Woyera ukutitsogolela kuchita.

Malingaliro amakhala mu chili chonse. Amafuna apeze malo oyika chili chonse kuti zizimveka bwino komanso ndi chosamalidwa. Sitimakonda mafunso osayankhidwa. Chida chimodzi chimene Mzimu umagwilitsa ntchito polipachika thupi lathu ndi mfunso losayankhidwa. Pamene *sitikudziwa* yankho, tikuyenela kumukhulupilira Mulungu kapena kudandaula ndi kuyesa kulingalira zinthu.

Mzimu Woyera ali ndi ntchito yobweletsa okhulupilira kumalo oti akule pamene apulumutsidwa. Mukhristu amene akhulupilira Atate pamene zinthu zisakuyenda bwino ameneyo ndi Mukhristu wamukulu. Ndiyeno choncho, Ambuye samatiyankha nthawi zonse mafunso athu chifukwa akutiphunzitsa ife kukhala okhulupilira. Choncho mukuyenera kukumbukira kuti maganizo anu ndi osiyana ndi dongosolo la Mulungu.

Malingaliro anu ndi achilengedwe ndiye ndi woyenera kukhala mbali imodzi ya thupi pokha pokha atakonzedwanso, kuphunzira *kuganiza mwa uzimu*.

Aroma 8 ikuyankhula za maganizo a thupi ndi maganizo auzimu. Agalatiya 5:17 (AMP) ikuti pakuti thupi lilakalaka potsutsana nalo thupi ndipo zizapitiliza kuyima ndi kutsutsana china ndi chinzake tibwelele kumaganizo athu ambuyo ku chiyambi cha ndimeyi.

Tikumbukile maganizo athu oyambira. Malingaliro a chilengedwe amafuna *kutiyika* ife penapake ndi kutiponyela ife mu chinthu choponyela zinyalala m'mene mungakhale zinthu zimene sitikuziziwa.

Tinali nalo bokosi la makalata limene linayikidwa pa ofesi pathu nthawi yina yake. Bokosi ili yonse inali ndi dzina la munthu wogwira ntchito pa ofesiyi. Pamene ndikufuna kutumiza ndondomeko kapena nkhani kwa munthu wina wogwira ntchito, ndimayika kachidziwitso mu bokosi la munthuyo. Kamodzi pa nthawi zina zimene ndamuuza munthu kuti achite samachita, pamene ndinayang'ana ndinapeza kuti ndinayika kachidziwitso ko malo osayenela. Pena kuyika malo oti mulibe kalikonse pamene palibe dzina liri lonse.

Mulungu anagwira ntchito pa mabokosi a makalatawa kundiphunzitsa mphunziro ili limene ndikuyesa kukuphunzitsani. Amandionetsa kuti m'mene ndinayika zinthu molakwika mu ofesi, inenso nthawi zina ndimayika zinthu molakwika m'mutu wanga. Nthawi zonse ndimafunitsitsa *kuyika* chili chonse m'maganizo anga kuti ndikhale ndi maganizo abwino omukhulupilira Mulungu. Ndinali ndi bvuto la likulu ndi "malingaliro." Ndimangofunsa "Chifukwa, Mulungu, Chifukwa?" Kenako ndinakhala ndi kusokonekela ndi kudandaula ndi kusowa kwa mtendere ndi chimwemwe.

Ndimadzinyenga ndekha nthawi zina, Ambuye wandiwonesela chifukwa nthawi zina ndimaganizira ndili ndi nkhani yina ndikuyiwelengela, ndiye ndimapeza kuti pamene nditasokoneza zinthu ingakhale nditaganiza mwatsopano kumvetsetsa kuti kodi ndinawelengela bwino, kuti zinalidi zitapezeka malo olakwika.

Mulungu anagwiritsa pa Miyambo 37 (AMP) kubweletsa choonadi kwa ine: “Usaziye se wekha wanzeru.” Ambuye anandiziwitsa kuti sindinali wanzeru olo pang’ono ndi m’mene ndikuganizira. Sindikunena za nzeru a m’mutu. Ndikunena za malingaliro athu – tili ndi zinthu zimene timaziwelengela.

Miyambo 3:5, 6 (AMP) ikuti:

“Dzimirani, khulupilirani Yehova ndi mtima wako wonse ndi nzeru zako zonse osacirikizika pa luntha lako olo kumvetsetsa kwako. Mu njira zako zonse, umlemekeze, umzindikire, ndipo Iye adzaongola mayendedwe ako.”

Mulungu akadziyika poyera sumakhala ndi chisokonezo kapena kudandaula, koma ukayesa kuganizira ndi kuziwelelengela uzingozungulila osadziwa choonadi. Ndime ya 7 (AMP) ikuti “Usadziyese wekha wanzeru.”

Izi ndi njira ziwiri zimene ungachite pa nyengo iri yonse. Imodzi ndi yokonza imodzi ayi. Wina ndi wauzimu pamene wina ayi. Ndingonena kuti wina wake wandipatsa uneneli umene sindikuyimvetsetsa, kapena kuti ndili ndi maloto auzimu amene sindikuwamvetsetsa ndingapite kwa Atate ndi kunena “Atate, sindikudzimvetsetsa izi. Ndikufuna ndimvetsetse ndiyeno ndikufunsa kuti mundipatse kumvetsetsa.”

Kenako ndinayika zinthu zimene sindimadzimvetsetsa pambali. Mwachidule, sindimaziganizilanso. Ndinaziyika m’manja mwa Mulungu. Ngati anga khale okonzeka kundipatsa kumvetsetsa, azazichotsa pambali paja ndikuzibweletsa ku chikumbutso changa. Yohane 14:26 ikuti, koma nkhoswe Mzimu Woyera amene Atate azamtuma m’dzina langa, iyeyo azaphunzitsa inu zonse, nazakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu. Azandiphunzitsa *kudziwa* pa chibvumbulutsa zinthu zimene sindinadziwe.

Njira ya chiwiri imene ndikhonza kuthetsa nyengoyi, ngati ndinali ndi uneneli kapena maloto amene sindimawamvetsetsa chingakhale kuyamba kuyesa kuwelengela. Ndingayankhule ndi anthu ena za nkhanio ndi

kumva maganizo awo. Ndikhonza kuona kuti anthu ambiri akhonza kukhala ndi maganizo osiyana, ndiye zikhonza kuwonjezela chisokonezo changa. Ngati ndapeza zina mwa izo ndathana nazo, ndingayambe kuchitapo kanthu. Koma ngati ndingaimo ndikukhala wachilungamo ndekha, ndikuyenela kunena ndiliba mtendere mkati mwanga. Pamene ndikuyesesa kupanga china chake chichitike cholingana ndi “maganizo” ndi maloto anga, uneneli kapena masonphenya, mapeto ake *ndizakhala pa mabvuto*.

Kumbukilani “malingaliro” amabweletsa kusokonekela. Sindikunena kuti tisamaganize za zinthu zina, koma pali kusiyana pa kulingalira pa zinthu zina kwa nthawi yayitali kuona ngati ungamvetsetse ndi kuyesa kuziwelengela kuti ndisokonekele kwambili.

Pamene ukumva kusokonekela, chimenechi chikhale chenjezo kwa iwe kuti ukuchita zinthu munjira yolakwika.

9



CHISOKONEZO CHIMABA CHIMWEMWE CHANU

Mundime yomalizayi, ndifuna nditsimikize kuti chisokonezo sichichokera kwa Mulungu. Ku 1 Akorinto 14:33 ikuti “Pakuti Mulungu sali Mulungu wachisokonezo.” Akolose 3:15 (AMP) ikuti ndipo mtendere wa Khristu ukhale “*woweruza*” olo uchite ufumu m’mitima yanu, ichi ndi chisankho cha miyoyo yathu. Mtendere, monga woweruza, ukakhazikika zimaonekela chimene chili m’kati cha chimene chili kunja.

Chisokonezo chimayang’anizana ndi mtendere. Chisokonezo chimatanthauza zonse kukhala pamodzi, kutsayerestedwa, kusakaniza mosokonekela, kulakwitsa chinthu china kenakonso china. “Mtendere” umatanthauza mundondomeko, yosasokonezedwa, kukhutitsidwa. Ngati munthu alibe mtendere, sangakhale ndi chimwemwe. Yesu ananena pa Yohane 10:10 (AMP) kuti sikudza mbala koma kuti ikabe, kupha, ndi kuononga. Ndadza ine kuti tikhale ndi moyo ndi “*kukhala nao wochuluka.*”

Zaka zapitazo ndimaganza kuti ndidzasangalala ndi Mulungu ndi kukondwa naye mu moyo wanga. Ngati Yesu anandifela ine sindingangokhala ndi moyo wokha komanso kusangalala nawo.

Pa Yohane 15 akuyankhula m’mene Yesu amaphunzitsa za kupilira ndi moyo, zikutanthauza kulowa mu mpumulo wa Mulungu. Pa ndime 1-10

amayankhula za kupilira mu moyo. Kenako pa ndime ya 11 (AMP) anati: **“Izi ndalankhula ndi inu kuti chimwemwe changa chikhale mwa inu, ndi kuti chimwemwe chanu chidzale.”**

Ndikumvela ngati akufuna ife tisangalale ndi moyo. Chisokonezo chimatiletsa kusaona chimwemwe ichi.

Pomaliza ndikufuna ndikulimbikitseni kupanga chisankho kukhala ndi chimwemwe osati chisokonezo. Chofunika ndi kusiya “*kulingalira*.” Nthawi zonse timapeza chigonjetso cha uzimu pamene talola kusiya zinthu zina zakuthupi. Chikhalidwe cha thupi ndi ”kuyesa kuziwelenga.” Chikhalidwe cha uzimu ndi ”kukhulupilira Mulungu kutipatsa yankho mu nthawi yake.”

Pamene tikusiya “*kulingalira*” ndikhulupilira kuti muzakolola mtendere ndi *chimwemwe*.

PEMPHERO LA CHIPULUMUTSO



Mulungu amakukondanani ndipo akufuna kuti kukhale pa ubale wabwino. Ngati simunamulandire Yesu ngati mpulumutsi, mukhoza kumulandira tsopano. Tsekulani mtima wanu kwa Yesu ndi kupemphera pemphero ili....

“Atate ndikudziwa ndakuchimwirani, mundikhululukire. Ndisambitseni. Ndikulonjeza kukhulupilira Yesu mwana wanu. Ndikukhulupilira anandifera – ananyamula machimo anga pamene anafa pa mtanda. Ndikukhulupilira kuti anauka kwa akufa ndipo ndikupereka moyo wanga kwa iye tsopano.

Zikomo atate chifukwa cha mphatso ya chikhulukiro ndi moyo wosatha. Ndithandizeni kukhala moyo wa inu mdzina la Yesu, amen.”

Monga momwe mwapempera mu mtima mwanu, Mulungu wakulandirani, wakuyeretsani ndikumasalani ku ndende ya imfa ya uzimu. Pezani nthawi ndikuwerenga mawu awa ndikufunsa Mulungu akulankhuleni pamene mukuyenda naye mmoyo watsopanowu.

Yohane 3:16

1 Akorinto 15:3 -4

Ayefeso 1: 4

Ayefeso 2: 8 – 9

1 Yohane 1: 9

1 Yohane 4: 14 – 15

1 Yohane 5:1

1 Yohane 5: 12 – 13

Pempherani kuti Yesu akuthandizeni kupeza mpingo wophunzitsa ndi kukhulupilira Baibulo kuti mulimbikitsidwe ndikukula muchiyanjano ndi Yesu Christu. Mulungu alinanu nthawi zonse akutsogolerani tsiku ndi tsiku ndipo akuwonetsani mmene mmene mukhalire mmoyo watsopano!

ZA OLEMBA BUKHULI



JOYCE MEYER wakhala akuphunzitsa Mau a Mulungu kuyambira 1976 ndiponso mu utumiki wa mphumphu kuyambira 1980. Iyeyo ndi munthu amene mabukhu ake agulitsidwa kwambiri oposela makumi asanu ndi awiri, kuphatikiza Kubvomeleza Kufunafuna Kupeza Mtendere (Approval Addiction in Pursuit of Peace), Tingamvetsele Bwanji kwa Mulungu (How to Hear from God), ndi Malo a Nkhondo M'malingaliro (Battlefield of the Mind). Watulutsanzo mazana mazana a makaseti omvotsela komanso kosungilako ma vidiyo kaseti. Mapologalamu a pa wayalesi ndi a pa kanema a Joyce a Kutsangalala Moyo Tsiku ndi Tsiku amaonetsedwa dziko lonse lapansi. Joyce amayendayenda madela ambiri kukatumikila. Joyce ndi mwamuna wake Dave, ali ndi ana anai akulu amene amakhala ku St. Louis, Missouri.